




MUTU 11:


PASKHA NDI
MASAUTSO A
KHRISTU



PITANI,
KAKONZENI
PASKHA KUTI
TIDYE.



NDAFUNA KUTI NDIDYE NANU
PASKHA UYU NDISANAYAMBE KUZUNZIKA.
SINDIDZADYANSO PASKHA WINA KUFIKIRA
UFUMU WA MULUNGU UTAKHAZIKITSIDWA
PA DZIKO LAPANSI. PAMENEPO MUDZADYA
PA TEBULO LANGA, NDIPO MUDZAKHALA
PA MIPANDO KUWERUZA MAFUKO
KHUMI NDI AWIRI A ISRAELE.




NDIKUUZANI CHINTHU CHINA,
KUTI CHIMENECHO CHIKACHITIKA
MUKHULLUPIRIRE. MAU A MULLINGU PA
MASALIMO 41:9 AKUTI, "IYE AMENE
ADYA NANE MKATE, WANDIKWEZERA
CHIDENDENE CHAKE." NCHIFUKWA
CHAKE NDIKUKUUZANI KUTI MMODZI
WA INU AMENE DZANJA LAKE LILI NDI
INE PA TEBULO LINO
ADZANDIPEREKA KWA ADANI.

ZOSATHEKA!

IZI ZAKHAZIKITSIDWA
KUTI ZITERO NDITHU,
KOMA TSOKA KWA
MUNTHU AMENE
ADZACHITA CHINTHU
CHIMENECHI.





AMBUYE KODI
NDINE? INE
SINDIKUFUNA
KUKUPEREKANI KWA
ADANI.

AMBUYE,
SINDINE,
SICHONCHO?

AMBUYE,
SINDINGAKUPEREKANI.

LUKA 22:8-23



NDI MMODZI WA
INU AMENE
AKUSUSA DZANJA
LAKE PAMODZI NDI
INE M'MBALEMU.



TONSEFE
TINASUSITSA
MKATE WATHU
M'MBALEMO.

YOHANE ANAYANKHULA
MOTSITSA MALI KWAMBIRI
NDIPO ANAPEMPHA YESU
KUTI AONETSE MUNTHU
AMENE ATI ADZAMUPEREKE.
YESU ANATI, "NDI IYE AMENE
NDIMPATSE CHIDUTSWA
CHAMKATE ICHI
NDIKACHISUSITSA M'MBALE."



AMBLIYE, KODI
NDINE?

WATERO.

YESU ANASUSITSA
MKATEWO
NAUPEREKA KWA
YUDASI.



CHIMENE
LIFUNA
KUCHITACHO,
CHITA
MWAMSANGA.




MATEYU 26:23-29;
YOHANE 13:26-30



KODI YUDASI
AKUPITA
KUTI?


AMBUYE AMUTUMA KUTI APITE
KWINA KWAKE MSANGA; POPEZA
NDI MSUNGICHUMA, NKUTHEKA KUTI
AKUKAPEREKA MATHANDIZO ENA
KWA ANTHU OSALUKA.



TSOPANO
NDILEMEKEZEDWA.
ANA ANGA,
SINDIKHALA NANU
LIMODZI NTHAWI
YAITALI.


SIMUNGATHE KUPITA
KUMENE INE NDIKUPITA.
TSOPANO NDIKUKUPATSANI
LAMULO LATSOPANO, LAKUTI
MUZIKONDANA. CHIFUKWA CHA
KUKONDANA KWANUKO, ANTHU
ONSE ADZADZIWA KUTI
NDINU OPHUNZIRA ANGA.

SIMUNGATHE KUPITA KUMENE
INE NDIKUPITA. TSOPANO
NDIKUPATSANI LAMULO LATSOPANO,
LAKUTI MUZIKONDANA. CHIFUKWA
CHA KUKONDANA KWANUKO, ANTHU
ONSE ADZADZIWA KUTI NDINU
OPHUNZIRA ANGA.



AMBUYE, NGAKHALE
ALYENSE ATAKUKANI,
INE NDEKHA
SINDINGAKUKANENI.


PETRO,
TAMBALA
ASANALIRE KAWIRI,
UDZAKHALA
UTANDIKANA
KATATU.



NDI BWINO KUTI
NDIDZAFE NANU
PAMODZI KULEKANA
NDI KUKUKANANI.


NDATEMETS
NKHWANGWA PA
MWALA, INE
SINDIDZAKUKANANI!

SANGACHITE
KUNDIKAKAMIZA
KUTI NDIKUKANANI.



MAU A MULLINGU AMANENA
MOMVEKA BWINO: NONSENU
MUDZANDIKANA. KOMANSO,
MNENERI YESAYA PONENA ZA INE
ADATI, "ANACHITA NAYE NGATI
KUTI ANALI WOCHIMWA."


PETRO,
UKADZATEMBENUKIRANS
O KU CHIKHULLUPIIRO
CHAKO MWA INE,
UDZALIMBIKITSE
CHIKHULLUPIIRO CHA
ABALE AKOWA.



WODALITSIKA NDINU,
AMBUYE MULLINGU
WATHU, MFUMU YA
DZIKO LONSE, AMENE
MUMATIPATSA
CHAKUDYA KUCHOKERA
M'NTHAKA.

MKATE UYU AKUIMIRA
THUPI LANGA LIMENE
LAPEREKEDWA KWA INU. NTHAWI
ZONSE MUKAMACHITA
CHIKONDWERERO CHA PASKHA,
MUZINDIKUMBUKIRA.


MATEYU 26:33-35; YOHANE
13:31-38; I AKORINTO 11:24-25



THUPI LANGA
LIDZANYEMEDWA
CHIFUKWA CHA
INU.

A comic book illustration depicting a scene with three men. In the center, a man with long brown hair and a beard, wearing a white tunic and an orange sash, sits and looks towards the man on his right. The man on the right has a beard and is wearing a blue and white striped tunic with a white hood; he is holding a small white object in his hands. The man on the left has a beard and is wearing a purple tunic, looking down at his hands. A speech bubble above the central man contains the text "TENGANI, IDYANI." The background is a textured, brownish wall.

TENGANI,
IDYANI.




CHIKHO ICHI CHA VINYO
CHIKUIMIRA PANGANO
LATSOPANO CHIFUKWA CHA
MWAZI WANGA LIMENE
LDZAKHETSEDWA POTSUKA
MACHIMO ANU.



GAWANANI NONSENU,
NDIPO MUMWE VINYO
YENSEYO.
SINDIDZAMWANSO CHIPATSO
CHA MPHESA KUFIKIRA
NDITADZAMWANSO NANU
MU UFUMU WANGA.


KUTSOGOLOKO
MUKAMADZACHITA ZIMENEZI,
MUZIDZAKUMBUKIRA IMFA
YANGA MPAKA
NDIDZABWERANSO.





MUSAVUTIKE KAPENA
KUCHITA MANTHA CHIFUKWA CHA
ZIMENE NDIKUKUUZANIZI. M'NYUMBA
YA ATATE ANGA MULI MALO AMBIRI.
NDIKACHOKA PAKATI PANU,
NDIKUKAKUKONZERANI MALO, NDIPO
NDIDZABWERANSO KUDZAKUTENGANI
KUTI MUKAKHALE NDI INE
KUMENE NDIKUPITAKO.

YOHANE 14:1-3; 1
AKORINTO 11:24-26



KOMA AMBUYE,
SITIKUDZIWA KUMENE
MUKUPITA, TSONO
TINGADZIWE BWANJI
NJIRA YOPITIRA
KWANUKO?




NJIRAYO MUMAIDZIWA,
CHIFUKWA INE NDINE NJIRA, CHOONADI
NDI MOYO. PALIBE MUNTHU AMENE
ANGAPITE KWA MULLINGU ATATE POPANDA
KUDZERA MWA INE. NGATI MUMANDIDZIWA,
NDIYE KUTI MUMADZIWANSO ATATE,
NDIPO MWAWAONA.




AMBUYE,
TIONETSENI ATATE
NDIPO TIDZAKHUTIRA.

FILIPO, WAKHALA NDI
INE KWA NTHAWI YAITALI,
KOMABE SUNDIDZIWA? UKAONA
INE, WAONANSO ATATE. INE
NDI ATATE NDIFE AMODZI.



SINDIKUSIYANI NOKHA.
NDIDZABWERA KWA INU. DZIKO
LAPANSI SILIDZANDIONANSO,
KOMA NDIKUTUMIZIRANI MZIMU
WOYERA KUTI AZIDZAKHALA
NANU NDI KUMAKUTONTHOZANI.
ADZAKHALA MWA INU NDIPO
ADZAKUTSOGOLERANI KU
CHOONADI CHONSE.

NGATI MUMANDIKONDA,
SUNGANI MALAMULO ANGA.
NDIDZAKUPATSANI MTENDERE
UMENE DZIKO LAPANSI
SILINGATHE KUKULANDANI.



MUKADANDIKONDA
MUKANAKONDWERA KUTI
NDIKUBWERERA KWA ATATE
ANGA. NDAKLUZANI ZINTHU
ZIMENEZI ZISANACHITIKE KUTI
MUTHE KUKHULUPIRIRA.

IMIRIRANI, TIYIMBE
NYIMBO NDIPO
TIPITA KUMUNDA
KUKAPEMPHERA.




YESU PAMODZI NDI
OPHUNZIRA AKE
ANAYIMBA NYIMBO
YOMALIZA.

MATEYU 26:30; YOHANE 14:5-10, 15, 25-30

TSATIRENI
MWAKACHETE
TE. TIPITA
KUKAPEMPERA
KU MALO ATHU
OBISIKA AJA.





MUSAVUTIKE CHIFUKWA
NDINANENA KUTI POSACHEDWAPA
NDICHOKA PAKATI PANU, NDIPO
KUTI SIMUDZANDIONANSO.

POPEZA NGAKHALE MUDZALIRA,
CHISONI CHANU CHIDZASANDUKA
CHIMWEMWE CHACHIKULU.
NDIDACHOKA KWA ATATE, NDIPO
POSACHEDWAPA NDIBWERERA
KWA ATATEWO.

TSOPANO
MUKUYANKHULA
MWACHINDUNJI.
TIKUKHULUPIRIRA.

KODI TSOPANO
MWAKHULUPIRIRA? POSACHEDWAPA
NONSENU MUDZANDISIYA
NDEKHANDOKHA NDIPO MUDZABALALIKA.
KHALANI POMANO, INE NDIKUPITA
UKO KUKAPEMPHERA.

ATATE, NTHAWI IJA YAKWANA.
NDAMALIZA NTCHITO IMENE
MUDANDIIZA KUTI NDIGWIRE.
NDIPO TSOPANO MUNDILEMEKEZE
NDI ULEMERERO WOMWE NDINALI
NAWO NDI INU DZIKO LAPANSI
LISANALEDGEWE. NDAWAPHUNZITSA
ZA INU NDIPO ALANDIRA MAI ANGA.
DZIKO LAPANSI LIDZADANA NAWO
MONGA MOMWE LACHITIRA NDI INE,
POPEZA NDIMAWAUZA CHOONADI PA ZA
MACHIMO AO. IWOWA SI A DZIKO LINO
LAPANSI AI. SINDIKUPEMPHA KUTI
MUWACHOTSE M'DZIKO LAPANSI,
KOMA KUTI MUWATETEZE KWA
WOIPAYO.





KOMANSO NDIKUPEMPHERERA
ONSE AMENE ADZANDIKHULUPIRIRA
CHIFUKWA CHA LIMBONI WAO. NDIKUFLUNA KUTI
ONSEWA AZIKHALA NANE MONGA MOMWE INE
NDIMAKHALIRA NDI INU. ATATE, LOLANI KUTI
CHIKONDI CHOMWE INU MUMANDIKONDA
NACHO CHIKHALE MWA IWOWA NDIPO
KUTI INE NDIKHALE MWA IWO.



MOYO WANGA
ULI NDI CHISONI
CHACHIKULU,
CHISONI CHODZETSA
IMFA.

MATEYU 26:31, 38; YOHANE
16:19-20, 17:1-10



ATATE, NGATI NKUTHEKA,
CHOTSERENI CHIKHO CHA MKWIYO,
UMENE NDIYENERA KUMWA.
KOMABE SINDIKUFUNA KUTI
NDICHITE KUFUNA KWANGA, KOMA
KUFUNA KWANU. NDIMWA NDITHU
CHIKHO CHAMKWIYOCHI NGATI
NKOYENERA KUTI NDITERO.

YESU ADABWERA M'DZIKO LAPANSI
KUTI ADZASENZE MACHIMO A ANTHU,
KOMA PAMENE NTHAWI YAKE INAFIKA,
ANAFUNA KUKANA MANYAZI A MTANDA,
CHIFUKWA ZIMATANTHAUZA KUTI IYEYO
AYENERA KUKHALA TCHIMO LA ANTHU
A PA NTHAWI ZONSE.




ATATE, NGATI
NKUTHEKA, CHIKHO
ICHI CHINDIPITIRIRE.

**KOMA OSATI
KUFUNA KWANGA;
KUFUNA KWANU
NDIKO KUCHITIKE.**




**YESU ANATULUKA
THUKUTA LAMBIRI
LAMWAZI.**



WOYERANU, NTHAWI
YA MAZUNZO ANU YAFIKA,
KOMA ATATE ALI NANU.
MAWA ONSE OKHALA
KUMWAMBA ADZAKHALA
AKUONERERA MOMWE
MUDZASENZERE MACHIMO
A PA DZIKO LAPANSI.

TINALIPOTU PAMENE
MUNKALENGA DZIKO
LAPANSILI; TIKHALAPONSO
PAMENE MUZILIPULUMUTSA.

POSAKHALITSA
MNGELO ANAFIKA
KUDZATUMIKIRA
YESUYO.



MASALIMO 23:5-6;
LUKA 22:41-44; AHEBRI
6:6; 12:2

MAWAMAWALI
SATANA
AGONJETSEDWA
NDIPO NGONGOLE
YAMACHIMO A
ANTHU ILIPIRIDWA.

ABRAHAMU NDI ONSE
OKHALA KU PARADIZO AKULINDIRA
KUBWERA KWANU. AKUKONZERANI
CHAKUDYA PAMASO PA ADANI ANU;
CHIKHO CHANU CHIKUSEFUKA.
ZONADI ZOKOMA NDI CHIFUNDO
ZIDZAKUTSATANI, NDIPO
MUDZAKHALA M'NYUMBA YA
MULUNGU MPAKA MUYAYA.

DZUKANI.
YUDASI, MWANA
WACHITAYIKO,
AKUBWERA
KUDZAKUPEREKANI
KWA ADANI.



ATATE, CHIFUKWA
CHA ZIMENEZI
NDINABWERA
M'DZIKO LAPANSI.



MWAGONA. KODI
SIMUNGANDILINDIRE KWA
ORA LIMODZI CHABE? DZUKANI,
NDIKUPEREKEDWA M'MANJA
MWA ANTHU OCHIMWA.



AMBLIYE,
NDAKONDWA
KUKUONANI KUNO.
KOMA NDIKUOPA
CHIFUKWA ENA
ANDITSATIRA.



YUDASI, KODI
UKUNDIPEREKA
KWA ADANI NDI
MPSOMPSONO?



**YUDASI!
MUNTHU
WACHIWEMBU!**

**MUWAPHE NGATI
AKULIMBALIMBA.**

**TADIKIRANI
KAYE! KODI
MUKUFUNA
YANI?**

MATEYU 26:40, 45-50; YOHANE 12:27, 18:1-4



**YESU WA KU
NAZARETE.**

NDINE.



**ONANI! ALI NDI
MPHAMVU!**

ASILIKALI ANKACHITA
MANTHA NDI YESU
NDIPO ANAGWA
CHAGADA.



NDI AMENEYO.
MUKUOPA
CHIYANI?
MGWIRENI!


*SIMUGWIRA
MBUYE WANGA.*



A comic book illustration of a man with a dark beard and mustache, looking upwards with a wide-eyed, desperate expression. He has a jagged, bloody wound on his neck. The background is a bright yellow, suggesting a dramatic or intense scene. The man is wearing a blue garment. The text 'FYUUUU!' is written in large, bold, white letters with a black outline, slanted upwards to the right.

FYUUUU!

MAYONEEEE!



**SIYANI! PASAKHETSEDWE
MWAZI PANO. PETRO, IKA
LUPANGA LAKO M'CHIMAKE.
NDIKADAFUNA NDIKANAITANA
ANGELO 10,000 KUTI ABWERE
ADZANDITHANDIZE. ILI NDI ORA
LA MDIMA.**

**WANDIDUL
A KHUTU!**

MUKUBWERA KWA INE NDI
MALUPANGA NGATI KUTI NDINE
WAMBANDA. NDINKAKHALA NANU
M'NYUMBA YA MULLINGU. BWANJI
SIMUDANDIGWIRE NTHAWI IMENE
IJA? NDIKUUZANI CHIFUKWA CHAKE.
IZI ZIKUCHITIKA KUTI MALEMBO
OYERA AKWANIRITSIDWE.






***MULLINGU
THANDIZENI!***



ILO,
LIKUONEKA
NGATI
LATSOPANO.



NDINE AMENE
MUKUFUNA.
SITILIMBALIMBA.
GWIRENI NDIPO
ALEKENI AWA
AZIPITA.



**NCHOZIZWITSA
NDITHU! WACHIRITSA
KHUTU LANGA!
WACHIRITSA KHUTU
LANGA!**



**AGWIRENI!
GWIRANI
ONSEWO! WINA
ASATHAWEPO!**

**TISIYENI
TIZIPITA.**

**OPHUNZIRA ONSE
ANATHAWIRA MU
MDIMA.**


**MATEYU 26:52-57; MARKO
14:51-52; LUKA 22:50-51**



TIYENI;
IZI TIKONZERETU
MSANGA ANTHU
ASANAMVE.

ANAMUBWERETSA YESU
KU MALO AMENE
ANSEMBE NDI ANTHU
OTI APEREKE LIMBONI
ANASONKHANA.


AMATI IWEYO
UMANENA KUTI NDIWE
MESIYA, NDIPONSO KUTI
MULLINGU NDI ATATE AKO.
UNKANENA KUTI SINDIWE
WA M'DZIKO LAPANSILI.
KWANU NKUTI?



NDAKHALA NDIKUPHUNZITSA
M'MASUNAGOGE NDI M'TEMPILE.
SINDINKAPHUNZITSA M'MALO
OBISIKA. NCHIFUKWA CHIYANI
MUKUNDIFUNSA ZIMENEZI?
AFUNSENI AMENE ADAMVA ZIMENE
NDINKAPHUNZITSAZO. AKUDZIWA
ZIMENE NDI MANENA.



PHAAA!



SUNGAYANKHE
MKULLU WA
ANSEMBE MOTERO.

NGATI
NDAYANKHULA CHOIPA,
CHITIRANITU LMBONI ZA
CHOIPACHO. KOMA NGATI
NDAYANKHULA ZOONA,
NCHIFUKWA CHIYANI
MUKLUNDIMENYA?



BWERETSANI
MBONI ZOTI
ZITSUTSE
MUNTHU UYU.

YOHANE 18:19-23



AMANENA KUTI ADZAONONGA
TEMPILE NDI KUIMANGANSO PA
MASIKU ATATU, KOMA OSATI
NDI MANJA AKE.

AI, AMANENA
KUTI WINA
ATAONONGA
TEMPILE, AKHOZA
KUIMANGANSO.

SIMUNALIPO. NDINAMVA ZIMENE
ADANENA. ANKANENA ZA IYE
PAMENE ANKANENA ZA KUONONGA
TEMPILE. NDIYESA ANKANENA ZA
KUONONGEKA KWA THUPI LAKE.



ZACHIBWANA NDITHU.
ANGAMANGENSO BWANJI
THUPI LAKE PATATHA
MASIKU ATATU?

SINDIKUDZIWA.
ANGADZUTSE BWANJI
TEMPILE PA MASIKU
ATATU OKHA?


KODI SUKUMVA
MMENE ANTHUWA
AKUKUTSUTSIRA?
SUYANKHAPO?






YESU
ANANGOKHALA
CHETE.

*MUNTHU
WOPUSA
SAYANKHA.*



NDIKUKULAMULA
M'DZINA LA MULLINGU
WAMOYO KUTI
UYANKHULE NDIPO
UYANKHE NGATI
NDIWEDI KHRISTU,
MWANA WA MULLINGU
WAMOYO.

NDINE MWANA WA
MULLINGU. NDIPO MUDZANDIONA
NDIKUKHALA KU DZANJA LAMANJA
LAMPHAMVU LA MULLINGU KENAKA
NDIDZABWERANSO M'DZIKO
LAPANSILI M'MITAMBO YA
MLENGALENGA.

A man with a long brown beard and a purple robe with yellow trim is shown tearing at a piece of purple fabric. He is looking upwards with a determined expression. The background is a simple yellow wall with some architectural lines.

SITIKUFUNANSO
MBONI ZINA. TAMUMVA NDI
MAKUTU ATHU. AKUNYOZA
MULLINGU POMANENA KUTI
IYEYU NDI MWANA WA
MULLINGU. AYENERA
KUPHEDWA BASI!

MMANGENI
M'MASO KUTI
TIONE KUTI NDI
MNENERI WANJI
IYEYU.

WANSEMBE ANANG'AMBA
ZOVALA ZAKE KUSONYEZA
KUTI ANAWAWIDWA MTIMA
KWAMBIRI.

MPANDENI.
ANANDIONONGERA
MALONDA ANGA
M'TEMPILE.

TIONE NGATI
ANGANENERE.

TIONE NGATI
ACHITE
CHOZIZWITSA





PHAAA!

MPANDENINSO!


PHAAA!

**TAONANI MMENE
WAFOOKERAMU!**

KHWAPU!

**NENERA NDIPO
LTIUZE AMENE
WAKUMENYA.
NDIYESA KUTI
UDALI MNENERI.**


**CHIZA MABALA
AKOWO. TIONETSE
CHOZIZWITSA.**



KENAKA, KUNJA KWA
TEMPILE, PETRO
ANKAMUTSATIRA
YESU CHAPATALI.

NDIKUKUDZIWA!
NDIDAKUONA ULI
NDI YESU. NDIWE
MMODZI MWA
OPHUNZIRA AKE,
SICHONCHO?

SINDIMUDZIWA
MUNTHU WOTCHEDWA YESUYU.
NDINGOFUNA NDIONE ZOMWE
ZIKUCHITIKA KUNO.



NDINAKUONA
USIKU M'MUNDA
MUJA! NDIWE
MMODZI NDITHU...

IWE, KODI NDIWE
WOPENGA? INETU
NDINE MSODZI CHABE.
SINDIMUDZIWA MUNTHU
WOTCHEDWA YESUYU.

MATEYU 26:67-70;
LUKA 22:64-65



INDE, NDIWE MMODZI
MWA OPHUNZIRA AKE.
NDINAKUONA UKUYENDA
NAYE KAMBIRIMBIRI.

KALEZADI!
CHING'ANING'ANIDI!
MBAMBAN'DUKE! MAI INU,
PA MOYO WANGA WONSE
SINDINAMUONEPO
MUNTHU AMENEYU.



KOKORIRIKOOOO
KOKORIRIKOOOO

TAMBALA AMENEYU
WALIRA MSANGA,
SICHONCHO?

AKUMUTULUTSIRA
KUNJA. AKUONEKA
KUTI AMUMENYA
KWAMBIRI.



AKUTI AMUTENGERA
KWA AKULLIAKULU A
BOMA KUTI
AKAMUWERUZE.

AKAMKWAPULA

PETRO, ATAMVA
TAMBALA AKULIA,
ANAKUMBUKIRA
MAU A YESU, KUTI
TAMBALA
ASANALIRE KAWIRI,
ADZAKHALA
ATAMUKANA
YESUYO KATATU.
ANACHITA
MANYAZI
CHIFUKWA CHA
MANTHA AKEWO.

ANTHU ACHINYENGOWA
AFUNA KUTI WINA NDIYE
ACHITE NTCHITO YAO
YONYANSAYI.

MATEYU 26:71-75, 27:1-2;
LUKA 22:58-62, 23:1




**MKWAPULENI NDI
MKWAPULO WA MINGA
ZISANU NDI ZIWIRI.**

**MULLINGU, NDAPHULAPO
CHIYANI. NDAMUKANA KATATU,
MONGA MOMWE ADANENERA.
ZACHITIKIRANJI ZIMENEZI?
AKUZUNZIKIRANJI?**

**FULLUMIRANI.
KUNJA KUKUCHA.**

**ATATE, PATSENI
MPHAMVU.**



UKUFUNA CHIYANI
TSOPANO? KODI NDALAMA
ZIMENE TINAKUPATSA CHIFUKWA
CHOPEREKA MBLUYE WAKO
SIZIDAKWANE?

NDASINTHA
MAGANIZO.
MUITANITSENI KUTI
MUMUMASULE NDIPO
NDIDZAKUBWEZERANI
NDALAMA ZANU.

ZIMENEZO NDI NDALAMA ZA MAGAZI,
ZODETSEDWA; SITINGAZIKHUDZE. MBLUYE
WAKO APHEDWA LERO LINO BASI. USAOPE
CHILICHONSE. TIDZAKUGWIRITSA NTCHITO
YOGWIRANSO OPHUNZIRA ENA AJA
KUTI TITHANE NAWO.



TENGANI NDALAMA
ZANU. SINDIKUZIFUNA.
SINDIKUPEZA
MTENDERE MUMTIMA
MWANGA.

NGWIIII!

NGWIIII!



WOPLUSA.

A man with a beard, wearing a blue tunic and a green cloak, is running through a rocky, wooded landscape. He is looking back over his shoulder with a distressed expression, his right hand raised to his forehead. The background features large, gnarled trees and a rocky cliffside. A speech bubble is positioned above him, containing text in a stylized font.

**SINDINGAKHALE
MOYO CHIFLUKWA
CHA ZIMENEZO.**

MATEYU 27:3-6

A man in a green tunic and white shirt is climbing a large, gnarled tree. The background shows a landscape with rolling hills, green bushes, and a castle on a hill under a blue sky. A speech bubble is positioned in the upper left corner of the frame.


MULLINGU,
VUTO LANGA
NCHIYANI?

NCHIFUKWA
CHIYANI
SINDIDADZILETS
E UMBOMBO
WANGAWU.



MWINA IMFA
IKHOZA
KUNDIPATSA
MTENDERE...





NDINAMUONA
KOMA PALIBE
CHIMENE
NDIKANACHITA
POFUNA
KUMULETSA.

FULUMIRANI,
TIDULE
CHINGWECHO;
MWINAMWAKE
AKADALI NDI
MOYO!



KOMA PAMENE
ANKAKWERA
MUMTENGOMO, MZIMU
WA YUDASI UNALI
UTAFIKA KALE M'MOTO
WA CHIONONGEKO.




AKAMAGWA
MUMUGWIRE KUTI
ANGAGWERE
KUPHOMPHO.

MATEYU 27:5




**ALI
PATALI!**



ZOSAKHALA
BWINO! WAPHULIKA
NDIPO ZAM'KATI
MWAKE ZAYENDERERA
M'MUNDA MONSEMO.

EEE;
ZODWALITSA.

ANENERI ADANENAPONSO
ZIMENEZI.



MWANDIBWERETSERA
CHIYANI, MUNTHU
WINANSO WOSOKONEZA?
MTENGENI NDIPO
MUKACHITE NAYE MONGA
MWA MALAMULO ANU.

AYENERA KUPHEDWA,
NCHIFUKWA CHAKE TABWERA NAYE
KWA INU. PAJA MUDATILETSA KUPHA
MUNTHU ALIYENSE WONYOZA MULLINGU
POMUGENDA NDI MIYALA, TSONO
TABWERA KUTI MUTILOLE TICHITE
NAYE MKULLU AMENEYU
MONGA KUFUNIKIRA.

WAPALAMUL
A CHIYANI?



AMATI NDI
MFUMU.

KODI
NDIWE MFUMU
YA AYUDA?


KOMATU LIFUMU WANGA
SIWAPANSIPANO. ZIKADAKHALA
CHONCHO, ATUMIKI ANGA
AKADAMENYA NKHONDO
POFUNA KUTCHINJIRIZA
MOYO WANGA.



KODI
TSONO NDIYE
KUTI NDIWE
MFUMU?

NDINABWERA M'DZIKO
LAPANSILI KUDZACHITIRA
LIMBONI ZA CHOONADI.
ALIYENSE AMENE NDI
WACHOONADI AMAMVA
ZIMENE NDIMAYANKHULA.





SANAPALAMULE
MLANDU WOTI
NKUPHEDWA NAWO.
MUKUFUNA NDICHITE
NAYE CHIYANI?

MPACHIKENI,
MPACHIKENI.

MCHOTSENI
PANO NDIPO
MUMUKWAPULE.

ZEKARIYA 11:12-13; MATEYU 27:8;
MARKO 15:14; LUKA 23:1-4; YOHANE
18:29-38; NTCHITO 1:18



NDIMUKWAPU
LE KANGATI?

AKUTI
UMUKWAPULE
KOFIKAPO;
MIKWAPULO
39.

TIONA
MMENE MLALIKI
AMAVUTIRA.

MKWAPULO WA ZINGWE ZISANU NDI ZINAI NDI MKWAPULO WAMTENGO WOTALIKA MAINCHI 18 WOKHALA NDI ZINGWE ZISANU NDI ZINAI ZACHIKOPA ZOTALIKA PAFUPIFUPI MITALA IMODZI (1 METRE), ZOMWE KUMAPETO KWAKE AMAMANGIRIRAKO TIZITSULO TAKUTHWA KAPENA TIMAFUPA.

WAAAAA!

KWAMBIRI!

TSOPANO
ANZAKE AJA
ALI KUTI?

SANAPEMPHE
KUTI
AMCHITIRE
CHIFUNDO.

HWAPU!

MWINA AFA NDI
KUKWAPULIDWAKU
NDIPO ZUZIZWITSA
ZAKE ZIJA
SITIZIONANSO.

35


36

37

38

39

LUKA 23:11; YOHANE 19:1






**MSANA WAKE
WAONONGEKERATU!**

**EYA, NTHAWI
YONSEYO
NDIMALAKALAKA
NTAMENYAPO
MFUMU.**



ANKATI IYEYU
NDI MFUMU.
MVEKENI
CHOVALA ICHI.

MFUMU IMAYENERA
KUKHALA NDI
CHISOTI CHAUFUMU.




HA HA HA ICHI
CHINGAKHALE
CHISOTI CHAUFUMU
CHABWINO.

ooo!



**ICHO, TENGANI
CHISOTI CHANU,
INU WAMKULUKULU.
HA HA HA.**

**MUIKE
BWINOBWINO
CHISOTICHO
PAMUTU
PAKEPO.**



TIKUKUVEKANI
CHISOTI CHAUFUMU INU
MFUMU YA DZIKO
LONSE LAPANSI.

AAAAAAA!




TSOPANO,
IMIRIRA
BWINOBWINO
MOONGOKA.

GWIRITSITSANI
CHISOTI CHANU,
MFUMU.

HA, HA,
MUKHALE NDI
MOYO WAUTALI,
MFUMU.

INDE, NGAKHALE
KUTI AFA USIKU
WOMWE LINO.



**MFUMU
YACHROMA
SISUNGA NDEVU.**



TSOPANO
NDIYE
AKUONEKA
NGATI MFUMU.



WANGOTI CHETE;
SAKUPEMPHA
CHIFUNDO. TIYENI
TIBWERERE NAYENSO
KWA PILATO.



ONANI MFUMU
YANU.


TILIBE MFUMU
INA KOMA
KAESARA
YEKHA.

TAONANI
MUNTHUYU.
MUFUNA NDICHITE
NAYE CHIYANI?

**MPACHIKENI,
MPACHIKENI.**



MTENGENI
MUKAMUPACHIKE.
SINDIKUMPEZA
WOLAKWA
MUNTHUYU.




MUKUTANTHAUZA
CHIYANI KUTI ALIBE
CHOLAKWA?
IYEYUTU AMATI
NDI MWANA WA
MULLINGU.




MWANA WA
MULLINGU?
MBWERETSENI
KUNO.

LUKA 23:13-22; YOHANE 19:4-8



NDIWE YANI?
BWANJI SUKUNDIYANKHA?
KODI UKUDZIWA KUTI NDILI NDI
MPHAMVU ZOLAMULA KUTI
UPHEDWE?

ATATE
AKUMWAMBA
ADAKAPANDA
KUKUPATSANI
MPHAMVUZO
SIMUKANAKHALA
NAZO.



NDIKUKUUZANI.
SINDIKUPEZA
CHOLAKWA
CHILICHONSE MWA
MUNTHUYU.
NDIMUMASULA.

NGATI
MUMUMASULA,
NDIYE KUTI
SINDINU
BWENZI LA
KAESARA.

**MPACHIKENI,
MPACHIKENI!**

MTENGENI NDIPO
MUCHITE NAYE ZIMENE
MUKUFUNA. NDILEMBA
MAKALATA ONENA ZA MLANDU
WAKE. KOMA MWAZI WA
MUNTHU WOLUNGAMAYU
USAKHALE PA INE.



**MPACHIKENI
WABODZAYO!**

**TSOPANO
ZUZIZWITSA
ZAKO ZIJA ZILI
KUTI?**

MATEYU 27:24; YOHANE 19:9-17



NDIKHULLUPIRIRA
KUTI WATHEKA
BASI.

KHUUU!

KHUUU!



DZUKA
NDINGAKUKWAPULE.

EI, IWE!
MTHANDIZE
KUSENZA
MTANDA
MUNTHUYU.

**BWANJI
MWASANKHA
INE?**




WALAKWANJI?

ANKAKONDA
ALIYENSE.

OO, YESU,
PEPA.

INU AKAZI A KU YERUSALEMU,
MUSALIRIRE INE. DZILIRIRENI NOKHA
NDI ANA ANU, PAKUTI NTHAWI IDZAFIKA
PAMENE ONSE OKHALA MU
YERUSALEMU ADZABISALA CHIFUKWA
CHA ZOSAUTSA NDIPO
ADZAPEMPHERA KUTI AFE.



YESU ANANYAMULA MTANDA WAKE
KUPITA NAWO PAMALO PAMENE
ANAPHEDWERA. PANALI MBAVA ZIWIRI
ZIMENE ZINANYAMULANSO MITANDA
YAO PA TSIKU LIMENELO.

PANALI AMBIRI AMENE
ANKAKONDABE YESU NDI
KUMAMULEMEKEZA, KOMA
ANKAOPA KUTI AYANKHULE
CHILICHONSE.

MATEYU 27:32; LUKA 23:26-33



IMWA ICHI,
CHIKUTHANDIZA
KUCHEPETA
ULULU WAKO.

AI, NDIYENERA
KUCHITA
CHIFUNIRO CHA
ATATE ANGA.

AKUGANIZABE
KUTI NDI
MWANA WA
MULLINGU.



MTAMBALI
TSENI
BWINO.

BWERETSANI
NYLUNDO NDI
MISOMALI.




MGWIRENI ZOLIMBA.
ASUNTHA NDI KUKHOMA KWA
KANTHAWI PANG'ONO CHABE.
MGWIRENI BWINOBWINO
MPAKA MISOMALI ILOWE
PAKATI PA MAFUPA MPAKA
KUKAFIKA KUMTANDAKO.

**AI!
MWANA
WANGA!**

KHOO!

KHOO!



UKUGANIZA
KUTI
NCHIFUKWA
CHIYANI IYEYU
AMAGANIZA KUTI
NDI MWANA WA
MULLINGU?

CHINA CHAKE
CHOKHUDZA UNENERI
WAKALEKALE.
SIZIKUNDIKHUDZA.

MATEYU 27:33-34



GWIRANI MIYENDOYI
BWINOBWINO.
PAMAFUNIKA KUKHOMA
MAULEMENDO ANGAPO
KUTI MISOMALI IDUTSE
PAKATI PA MAFUPA.




MARIYA,
SINDINGAPIRIRE
ZOTEREZI.

SINDIMAGANIZ
A KUTI ZIFIKA
PAMENEPA.

*KOKA,
WOPANDAPAKE
IWE.*

INE
SINDIKANAVUTIKA
NACHO
CHIMENECHO, INU
ANTHU AULESI.



ATATE,
AKHULULUKIRENI
CHIFUKWA
SAKUDZIWA
ZIMENE
AKUCHITA.

YOHANE,
NDAKONDWA
KUTI ULI PANO.
NDI ZOOPSA
KWAMBIRI.

TONSE
TINAMUSIYA
YEKHAYEKHA.

ZEKARIYA 13:6;
LUKA 23:32-34



AI USATERO.
TIWANG'AMBE
PANAI.

AWA NDI MALAYA
AKE. INE
NDITENGA AWA.

TISAGAWANE
AWA. NDI
OSOKEDWA
BWINO.


TICHITE MAERE
CHIFLUKWA CHA
AMENEWA.

MALEMBO OYERA ANANENERATU
KUTI ADZAGAWANA CHOVALA CHAKE
NDIPO CHINA ADZACHITIRA MAERE.



WOPAMBANA
NDIYE
ATENGA.

TAONA, LEO,
MAGAZI
AKUKUTHONYERA.



ANAPULLUMUTSA
ENA. SANGATHE
KUDZIPULLUMUTSA
YEKHA.

EYI, YESU, UMATI
UKHOZA KUONONGA
TEMPILE NDI
KUIMANGANSO PA
MASIKU ATATU.
DZIPULLUMUTSE WEKHA
NDIPO TSIKA
PAMTANDAPO.



TSOPANO KHRISTU,
MFUMU YA ISRAELE,
ATSIKE PAMTANDAPO
KUTI TIONE NDI
KUKHULUPIRIRA.

WONAMA!

AMAKHULUPIRIRA KUTI
MULLINGU
ADZAMUPULUMUTSA.
MULLINGU AMUPULUMUTSE
TSOPANO, POPEZA
ANKAKONDWERA MWA
WONAMA! MULLINGUYO.

MASALIMO 22:18; MATEYU
27:39-43; YOHANE 19:23-24

IMWA ICHI,
CHIDZACHEPE
TSA ULULU
WAKO.

AI.



**NGATI NDIWE
MWANA WA MULLINGU,
DZITSITSE PAMTANDAPO
NDIPO IFE TIKUPHA
ENA MWA AROMA.**

**NCHIFUKWA
CHIYANI
UKUYANKHULA
CHIPONGWE
CHOTERO? KODI
SUOPA MULLINGU,
PODZIWA KUTI ULI
PAFUPI KUFA?**



IFE TIKULANDIRA
ZOTIYENERA,
KOMATU UYU NDI
YESU. SANALAKWE
CHILICHONSE.

YESU,
MUNDIKUMBUKIRE
PAMENE MULOWA
MU UFUMU
WANU.



LERO LOMWE
LINO UDZAKHALA
NDI INE
M'PARADIZO.



YOHANE,
USAMALE
AMAI ANGA.

NDITERO.


OO YESU,
WALAKWA
NJI?

MASALIMO 69:21; LUKA
23:36-43; YOHANE 19:25-27



KUNAGWA MDIMA NGATI USIKU KWA MAORA ATATU
PAMENE YESU ANALI CHIKHOMEDWERE PA
MTANDA. LINALI ORA LA MDIMA. MUNTHU
WOTCHEDWA YESU KHRISTU ANKAFAPA MTANDA
CHIFLUKWA CHA MACHIMO A PA DZIKO LAPANSI.

PAMENE YESU
ANANYAMULA
KATUNDU YENSE WA
MACHIMO, ANAFULLA:



MULLINGU WANGA,
MULLINGU WANGA,
MWANDISIYIRANJI
INE?

MULUNGU ANASANDUTSA YESU KUKHALA

WOSHIMWA M'MALO MWATHU.

ATATE,
NDIKUPEREKA
MZIMU WANGA
M'MANJA MWANU.

OO YOHANE,
AKUMWALIRA!
SINDIKUKHULUPIR
IRA KUTI
AKUMWALIRADI!

KWATHA!

MATEYU 27:45-50;
LUKA 23:44-46;
YOHANE 19:30; 2
AKORINTO 5:21

NDIPO
ANAMWALIRA.



MWADZIDZIDZI KUNADZA
CHIVOMEZI CHACHIKULU.

NDI CHIFUKWA
CHA YESUYU,
MFUMU YA AYUDA.
PAJATU ANKACHITA
ZUZIZWITSA.

CHIKUCHITIKA NDI
CHIYANI? POYAMBA
KUNAGWA MDIMA NGATI
USIKU, NDIPO
TSOPANO NTHAKA
IKUGWEDEZEKA.

SAKUCHITANSO
ZODABWITSA
TSOPANO.
WAMWALIRA.



KUKUYERANSO.
LERO NDI TSIKU
LODABWITSA NDITHU.


INDE ZONSEZI
ZIKUCHITIKA
MUNTHUYU
ATANGOMWALIRA.



ZOONADI,
MUNTHUYU
ANALI MWANA
WA MULLINGU.

AKUTI TIPHWANYE MIYENDO
YAO. AKUFUNA KUTI AKHALE
ATAMWALIRA NDI KUCHOTSEDWA
PA MITANDA YAO DZUWA
LISANALOWE. MAWA NDI LIMODZI
MWA MASIKU OYERA.

ANENERI ADANENAPO KALE
ZOTI ADZAKHOMEDWA PA
MTANDA NDIPONSO KUTI
MAFUPA AKE M'THUPI LAKE
SADZAPHWANYIDWA. CHONCHO
IZI ZINAKWANIRITSIDWA.



MUSAPHWANYE MIYENDO
YAKE. WAFKA KALE. KODI MUKUDZIWA
ZIMENE ANANENA ASANAFE? ANAPEMPHA
ATATE AKE KUTI ATIKHULULUKIRE
CHIFUKWA CHOMUPHA. AKUTI MUNTHU
UJA ANKACHITA ZOZIZWITSAYU
ANALI WOLUNGAMA.



PHWAA!


MASALIMO 34:20; ZEKARIYA 12:10;
MATEYU 27:54; YOHANE 19:31-37

CHONCHO ASILIKALI AJA
ANADUTSA YESU NAPHWANYA
MIYENDO YA MBAVA ZIJA.



SANAPHWANYE
MIYENDO
YAKE.

MARIYA, NDIYESE NGATI
NDINGAPEZE CHITHANDIZO
KUTI TIKONZEKERE ZOMLIKA
M'MANDA YESU.



SABATA LIMAYAMBA DZUWA
LIKAMALOWA. CHONCHO
NTHAWI INKATHA.
ANAYENERA KUFULLUMIRA
KUIKA THUPILO M'MANDA.



SABATA LIYAMBA
POSACHEDWAPA.
TIKAMUIKA
M'MANDA ANGA
ATSOPANO.

YOSEFE, MUNTHU
WOLEMERA, AMENE
SANALI MMODZI
MWA OPHUNZIRA
KHUMI NDI AWIRI
AJA, ANADZIPEREKA
KUIKA THUPI LA
YESU M'MANDA.

ZIKOMO KWAMBIRI,
YOSEFE. NDINU
BWENZI LABWINO.



<https://goodandevilbook.com/>